

KHALANI OTSIMIKIZA ZA MULUNGU



Ndipo Iwo akuwerengeka monga chonchi.

Ndipo Eliya Mtisibe, yemwe anali... wokhala ku Gileadi, anati kwa Ahabu, Monga YEHOVA Mulungu wa Israeli alimoyo, amene ndimakhala pamaso pake, sipadzakhala mame kapena mvula zaka zitatu izi, koma molingana ndi mawu anga.

Ndipo mawu a YEHOVA anadza kwa iye, kuti.

Choka kuno iwe, ndipo tembenukira iwe chakummawa, ndipo ukadzibise wekha cha kumtsinje wa Sidreki—Keriti, (ine ndimatanthauza kuti ndinene) umene uli usanafike ku Yordani.

Ndipo kudzakhala, kuti iwe uzikamwa a mu mtsinje; ndipo ine ndalamulira makungubwe kuti akudyetse iwe...

Chotero iye anapita ndipo anakachita molingana ndi mawu a YEHOVA: pakuti iye anapita ndipo anakakhala pafupi ndi mtsinje wa Keriti, womwe uli usanafike ku Yordani.

Ndipo makungubwe anambweretsera iye mkate ndi nyama mmawa, ndi mkate ndi nyama madzulo; ndipo iye ankamwa a mu mtsinje.

Ndipo zinafika pochitika patapita kanthawi, kuti mtsinje unaphwera, popeza munalibe mvula m'dzikolo.

Ndipo mawu a YEHOVA anadza kwa iye, kuti,

Nyamuka, ndipo upite iwe ku Zarefati, wa ku Zidoni, ndipo ukakhale kumeneko: taona, ine ndamlamulira mkazi wamasiye kumeneko kuti azikakudyetsa iwe.

Chotero iye ananyamuka ndipo anapita ku Zarefati. Ndipo pamene iye anafika pa chipata cha mzindawo, taonani, mkazi wamasiye anali pamenepo akutola nkhu: ndipo iye anaitana kwa iye, ndipo anati, Kanditengere ine, ine ndikukupempha iwe, madzi pang'ono mu chikho, kuti ine ndikhoze kumwa.

Ndipo pamene iye anali kupita kuti akawatenge iwo, iye anaitana kwa iye, ndipo anati, Kandibweretsere ine, ine ndikukupempha iwe, kanthongo ka mkate mu dzanja lako.

Ndipo iye anati, Monga Yehova Mulungu wako alimoyo, ine ndiribe mkate, koma kaufa ka mdzanja mu mbiya, ndi mafuta pang'ono mu msupa: ndipo, taona, ine ndiri kutola nkhuhi ziwiri, kuti ine ndipite umo ndi kukaziphikira izo kwa ine ndi kwa mwana wanga, kuti ife tikhoze kudya izo, ndi kufa.

Ndipo Eliya anati kwa iye, Usachite mantha; pita ndipo kachite monga iwe wanenera: koma kandipangire ine kwa izo mkate wawung'ono choyamba, ndipo ubwere nawo iwo kwa ine, ndipo kenako udzipangire uwelwa ndi...mwana wako.

Pakuti atero Yehova Mulungu wa Israeli, Mbiya ya ufa siudzatha, ngakhaleenso nsupa ya mafuta siudzauma, kufikira tsiku limene Yehova adzatumiza mvula pa dziko lapansi.

Ndipo iye anakalowa mkati ndipo anakachita molingana ndi kunena kwa Elisha: ndipo iye, ndi uyo, ndi a mnyumba ake, anadya masiku ambiri.

Ndipo mbiya ya ufa siinathe konse, ngakhaleenso msupa ya mafuta kuuma, molingana ndi mawu a Yehova, amene anayankhulidwa ndi Eliya.

Poti ndiyankhule mmawa uno, basi ndisanapite kutsidya kwa nyanja, ine ndasankha mutu, wotere: *Khalani Otsimikiza Za Mulungu.*

² Ndipo tsopano, Ambuye, dalitsani Mawu Anu pamene Iwo aziperekedwa, ndipo mulole Mzimu Woyera ugwire malingaliro athu ndi zoganiza zathu, ndipo mutikonzeketse ife kudzatichezera Kwake, monga ife tamupempha Iye kuti abwere. Pakuti ife sitimabwera ku nyumba ya Ambuye kuti tidzawonedwe, kapena kuti tidzawone, koma kuti tidzaphunzire za Inu, ndi kuti tidziwe za chikhalidwe Chanu, ndi njira Yanu, ndi zifukwa Zanu, kuti ife tikhoze kumakomana nazo zovuta za moyo, ndi chitsimikizo chenicheni, pokhala otsimikiza za Mulungu. Perekani izi, Ambuye. Mu Dzina la Yesu ife tikupempha izi. Amen.

³ Iwo uyenera kuti unali mmawa woopsya. Iko kunali kotentha kwambiri ndi kwafumbi, ndipo anthu anali mu msewu, anjala, ndipo pansu panali potentha kwambiri ipo panali pokonzeka kuti payake. Zonse izi zinali chinyezimiritsa cha machimo awo ndi kuvunda kwa makhalidwe awo.

⁴ Inu mukuona, Ahabu anali akulamulira mu—mu Israeli, pa nthawiyo, kapena pa Israeli, ndipo iye anali woyipisitsa wa mafumu onse a Israeli. Uko kunali kulibe mfumu yoyipa monga Ahabu, pakuti iye, pokhala ataphunzitsidwa ndipo akudziwa bwinoko, iye sanalephere kupitiriza kuti asamamukondweretse Mulungu mu chirichonse chimene iye ankachita. Ngakhale iye anali ndi dongosolo lalikulu la ankhondo, ndipo anthu anali

atalemera kwambiri pansi pa kulamulira kwake, koma, apobe, iwe sungakhoze kusamukondweretsa Mulungu ndi kuyembekeza kuti udutse nazo motalika kwambiri.

⁵ Ndiyeno, mu chikwati chake, mmalo mokwatira pakati pa anthu ake omwe, iye anapita uko ndipo anakakwatira wochimwa, wamafano, wopembedza mafano. Iye anakwatira Yezebeli. Ndipo iye sanali wokhulupirira.

⁶ Ndipo palibe wokhulupirira ayenera kumakwatira wosakhulupirira, mwanjira ina iliyonse. Nthawizonse ayenera kumakwatira okhulupirira.

⁷ Koma Ahabu anali atachita chinthu choipa ichi. Ndipo mopanda kukaika koma kuti Yezebeli anali mkazi wokongola. Ndipo iye anagwera chifukwa cha momwe iye ankawonekera, mmalo mwa chimene iye anali. Alipo anthu ambiri, amene amapanga kulakwitsa komweko, mpaka tsiku lino.

⁸ Ndipo iye anabweretsa kupembedza mafano mu fukolo, pakati pa anthu. Ndipo anthuwo, ansembe, atumiki awo, anali atagwera mu msampha wa chofunika chotchuka chachikulu ichi.

⁹ Ndipo ndicho chithunzi kumene cha dziko lathu lero. Ife tagwa pansi pa chofunidwa motchuka. Palibe kukaika kuti ansembe ankaganiza kuti izo zikanakhala zabwino basi, bola ngati boma lawo likuvomereza izo. Koma ine sindikusamala zimene boma liloleza, izo ziyenera kukhala chimene Mulungu akuloleza. Ndipo anthu ankaganiza kuti izo zikanakhala zabwino ngati iwo akanati aziyembekeza nawo mu zina za zinthu zachidziko.

¹⁰ Ndipo wina akhoza kundifunsa ine kuti ndibweze zimene ine ndangoyankhula, kuti icho chinali chithunzi chofanana ndi cha lero. Ife mwina sitingaganize kuti ndife opembedza mafano, koma ife tiri. Ndipo boma likuvomereza izo. Anthu lero ndi opembedza mafano, chifukwa iwo—iwo akupembedza mafano. Ena a iwo akupembedza akatswiri apa kanema, ngati mafano. Ena akupembadza ndalama, ngati mafano. Ndipo ena akupembeza akatswiri apa televizioni, ngati mafano. Koma chonse chimene iwe umayika patsogolo pa Mulungu ndicho fano, icho chikhoza kukhala chirichonse chimene icho chingakhale.

¹¹ Ngakhale Satana, mdani wathu wamkulu, ndi wanzeru chotero, mpaka iye amaikanso, nthawizina, mpingo patsogolo pa Mulungu. Iwe ukhoza kukhala ndi mpingo waukulu. Iyo ikhoza kukhala nyumba yaikulu, kapena icho chikhoza kukhala chipembedzo chachikulu. Ndipo, kachiwiri, ilo likhoza kukhala gulu lalikululu, koma musalole kanthu kabwere patsogolo pa Mulungu, mu mtima mwanu. Chirichonse, ndipo patsogolo pa Mulungu, ndi fano.

¹² Ndipo anthu awa ankadziwa kuti iwo sanali auzimu monga iwo anali kukhalira, pansji pa kulamulira kwa mafumu ena.

Ndipo iwo ankaganiza, basi chifukwa iwo anali fuko lauzimu, kuti chirichonse chikanakhala chabwino. Ndipo ndi momwe ife tabwerera pa malo amenewo panonso.

¹³ Miyezi ina yapitayo ine ndinali kuyankhula kwa bwenzi wabwino kwambiri wa ine. Ndipo iye anati, “M’bale Branham, ine ndikukhulupirira kuti inu mumakanikizira pansi United States uyu mwapafupi kwambiri.” Iye anati, “Inu nthawizonse mumakhala mukubangulira pa tchimo ndi momwe Mulungu ati adzalangire fuko lino.”

¹⁴ Ine ndinati, “Iye ayenera kuti achite izo, polinga kuti akhale wolungama.”

Iye anati, “Koma, M’bale Branham, inu mukuiwala kuti fuko lino linakhazikitsidwa pa Malemba. Ndipo makolo athu anabwera kuno, ndipo Mulungu anatipatsa ife cholowa ichi. Ndipo ife ndi fuko lachipembedzo.”

¹⁵ Ine ndinati, “Izo ndi zoono, zonse za izo. Ndipo palibe mmodzi yemwe amadziwa momwe ine ndimayamikirira fuko lino! Koma, penyani, m’bale wanga, Israeli nayenso anali wosankhidwa wa Mulungu, ndipo Iye anamutumizira iye aneneri ndi anthu aakulu. Koma Mulungu sangakhoze kupirira nalo tchimo. Iye anamupangitsa Israeli kukolola njere iliyonse imene iye anaifesa. Ndipo ngati Iye anamupangitsa Israeli kukolola chimene iye anafesa, Iye atipanga ife kuti ticolole chimene ife tafetsa.” Iye si wolemekeza munthu.”

¹⁶ Ndipo ife tafika pa malo akuti tikuganiza kuti chifukwa ife tikupumula pa chimene makolo athu anachita, kapena pa chimene oyambitsa athu aakulu a mipingo yathu, chimene nsembe yawo yaikulu inali kwa Mulungu, chimene chiri chabwino ndi choyamikiridwa kwakukulu chotero, koma ife sitingakhoze kupeza chipulumutso kuchokera mu chimene iwo anachita! Chipulumutso ndi chinthu cha payekha pakati pa munthu aliyense ndi Mulungu. Osati pa fuko, ndi mpingo wathu, koma ndi ifeeni pamaso pa Mulungu, ife timayankhira.

¹⁷ Izo zafika pa malo mu dziko lathu, mpaka pakati pa anthu auzimu kwambiri omwe amene ife tiri nawo, iwe ukati upite kwa amuna auzimu ndi aakazi, ndipo iwe umakapeza mu mtima mwawo kuti muli chinachake chimene chikusowa.

¹⁸ Ife takhala tiri, mu masabata pang’ono athawa, ine ndakhala ndikudutsa pa zina za zinthu izi, ndipo ndapeza kuti mwa anthu amene ine ndimaganiza kuti anali ngale, komabe ine ndapeza kuti iwo akuyika kutsimikizira pa zinthu zosakhalitsa, akumapita pozungulira ndi kumati, “Mulungu wandipatsa ine chachikulukulu *chakuti-n-chakuti*. Mulungu wandipatsa...” Inu mukupusitsana.

¹⁹ Zinthu zazikulu zogwirika nthawizonse sizimagona mu chifuniro cha Mulungu. Mulungu amapanga mvula kuti igwere pa olungama ndi osalungama. Koma chimene dziko

likusowa lero si chikhulupiriro chopusitsana, kuti uziyesera kudzipusitsira wekha mu chinachake ndi kumachitcha icho chazimu.

²⁰ Nthawizina chikhulupiriro chikhoza kuchita zozizwitsa zazikulu, ndipo komabe izo nkusakhala zikuchokera mu mtima wauzimu. Kodi Ambuye wathu sanati? “Ambiri adzadza kwa Ine, tsiku limenelo, ndi kuti, ‘Kodi ine sindinachite *ichi* ndi *icho*, mu Dzina Lanu?’ Ndipo Ine ndidzavomera kwa iwo, ‘Chokani kwa Ine, inu antchito ya kusaweruzika.’” Kodi kusaweruzika ndi chiyani? Ndi chinachake chimene iwe umadziwa kuti uchite molondola ndipo nkusachichita icho. “Ine sindinakudziwepo iwe konse,” Iye adzatero. Ndipo ife tiri kukhala mu tsiku limenelo.

²¹ Chimene ife tikusowa lero si katundu wochuluka wa zinthu zogwirika. Ife tiri nazo izo. Ife sitikusowa mipingo yaikulu. Ife sitikusowa magulu aakulu. Ife sitikusowa zochuluka pa wailesi ndi pa televizioni. Ife sitikusowa zochuluka kwambiri za zinthu izi. Koma chimene ife tikusowa lero, kuti tikhale auzimu, ndi munthu yemwe angati adzichepetse yekha pamaso pa Mulungu, ngati iwo alibe kobiri lirilonse, ndipo akhoza kupemphera mpaka mzimu uwo mkati mwa iwo utakhutitsidwa ndi ubwino wa Mulungu, ndipo chitsitsimutso nkumachitika mkati mwa mtima mwawo, izo zimasintha kachitidwe kawo ndi mkhalidwe wa pamene iwo akukhalapo.

²² Inu mukhoza kusakhala ndi nsapato ku mapazi anu, inu mukhoza kumavala nsanza, koma chinachake mu mtima mwanu chikuimba nthetemya za Mulungu. Ine kulibwino ndikhale ndi izo kuposa ndalama zonse za mdziko.

²³ Chotero inu simungakhoze kunena kuti zinthu zachirengedwe ziri nthawizonse chisonyezo cha madalitso a Mulungu. Davide anayankhula izo kwa Ambuye, kuti iye anali atawawona oyipa akuyangitsa zake... munga mtengo waukulu wa thundu. Koma Mulungu anamufunsa iye, “Kodi iwe unayamba wamulingalira iye pa mathero?” Ziribe kanthu ubwino wa zovala zomwe ife timavala, kaya nzochuluka bwanji tiri nazo kuti tizidya, izo si zimene zimapita mu Kukhalapo kwa Mulungu. Thupi ili limene ife tiri kukhalamo, limaonongeka, mopanda kusamala momwe ilo liri kusamaliridwa. Koma ndi solo yomwe ili mwa munthu; ndi chikhaliidwe cha mzimu chimene chimasunthira mu Kukhalapo kwa Mulungu wamoyo.

²⁴ Koma ife timangozitenga zinthu mwa chizolowezi. Ife timaganiza kuti basi chifukwa ife ndife fuko... Chomwechonso anali Ahabu ndi Israeli yense, mu tsiku limenelo, anali atatenga zinthu mwa chizolowezi, kuti chirichonse chinali bwino bwino. Ansembe awo ndi alaliki anali kuyesa kumawauza iwo, “Zonse ziri bwino. Chirichonse chiri bwino basi.” Koma iwo anali naye mmodzi, iye ankafuulira motsutsa chinthu cholakwika, chifukwa mmodzi yu ankadziwa kuti Mulungu

woyera sakanakhoza kukhutitsidwa ndi kachitidwe kamakono ka chipembedzo chosayera.

²⁵ Chomwechonso Mulungu Wakumwamba akadali yemweyo lero. Mu kuyesetsa kwathu konse ndi zinthu zazikulu zimene ife tikuyesera kuti tichite, Mulungu sadzakhala wosangalatsidwa konse kunja kwa moyo wathunthu woyeretsedwa pamaso pa Iye.

²⁶ Ife tikhoza kumanga masukulu, ndi zikumbutso, ndi makachisi. Ife tikhoza kukhala nao mabungwe. Ife tikhoza kuchita zinthu zazikulu, komabe Mulungu sangakhoze kukhala wokhutitsidwa mpaka moyo wa munthu utakhala woyeretsedwa pa guwa la Mulungu, kupatulidwira ku ntchito ya Mulungu. Ndipo inu simukuzipeza izo panonso.

²⁷ Iwe umapeza misonkhano yathu ya mapemphero ili yofooka kwambiri, pafupi miniti yokha ya pemphero, walumphira pa bedi. Ife tikupeza kuti izo zimachitika pafupi kamodzi kapena kawiri pa tsiku. Pamene, tonse ife tiri olakwa. Fuko lathu, mwachikhalidwe, liri kuvunda. Ife tiri nawo ma Billy Graham ndi ma Oral Roberts kulikonse. Koma mpaka patafika kuchita ludzu mu mtima wa Amereka, kuti umubweretse iye kwa Mulungu wamoyo kachiwiri, kwa chomuchitikira chamoyo, kwa chikhulupiriro chosafa mwa Mulungu wamoyo. Ife tikungomenyetsa ubongo wathu, monga izo zikanati zinenedwere, kunja.

²⁸ Ife tikhoza kumayenda ndi chidali chathu panja, ndi makolala athu atatembenuzidwira kumbuyo, ndi kumayenda pansu mu msewu, ndi kumakhumba kuti tizitchedwa “Dokotala” kapena “Arevi.” Ife tikhoza kumachitira ubusa mipingo yaikulu kwambiri imene ilipo mu dzikolo, ndipo ife tikhoza kukhala achipembedzo monga ife tikanakhoza kukhalira, mwakuti palibe munthu akanakhoza kuika chala pa moyo wathu. Koma mpaka solo iyo imene ili mkati mwa ife itakhala pa moto kufuna Mulungu, mpaka chinachake mkati umo, chimene chikulirira mofuna Iye! “Monga mbawala ipumira pofuna mtsinje wa madzi, moyo wanga ukuchita ludzu pofuna Inu, O Mulungu.” Mpaka ife titafika ku chotichitikira cha mtundu umenewo!

²⁹ Chotero, chikominisi, ndi zina zotero, zitenga malo monga izo zikuchitira, ndipo kujowina konse kumene ife tingakhoze kuchita sikudzakhoza konse kuimitsa izo. Izo zanenedweratu kuti zibwera. Koma Mulungu akuitanira ku Mpingo Wake.

³⁰ Momwe kuti mkazi wamng’ono uyu ayenera kuti anali wa chikhalidwe chonga cha Eliya! Chifukwa, kawirikawiri zochita zako zimasonyeza chimene iwe uli. Ndipo, kachiwiri, iye anali atasankhidwa kuti asangalatse mneneri wa Mulungu. Kumbukirani, iye anali Wamitundu, osati Myuda.

³¹ Ndipo dziko linali likuyaka. Ndipo mopanda kukaika kuti mkazi wamng’ono uyu, pokhala wa khalidwe limenelo, pokhala wa mtundu wa wokhulupirira... Pakuti ife tikuona

kuti Mulungu sakanati ayitanire kwa iye, ngati iye akanati asakhale woyenera kuti asangalatse mneneri wa Mulungu. Pakuti Iye sakanati atumize mneneri Wake ku nyumba imene inali yosayenera.

³² Iko sikunali kusankha kwake. Iko kunali kusankha kwa Mulungu. Iko sikunali kuitana kwake. Iko kunali Mulungu akumuitana iye. Iye anali ataikidwa mmphepete mwa mtsinje. Akhungubwe anali akumudyetsa iye. Koma uko kunali kulamulira kwa Mulungu kuti chinachake chichitike. Ndipo Mulungu ndithudi anapita kwa wokhulupirira wa chikhaliidwe chofanana ndi cha Eliya.

³³ Iye anali mkazi wamasiye. Ndipo ife tonse tikudziwa chimene iye, mkazi wamasiye, akanati azidutsamo nazo, ndipo mwamuna wake atafa ndi mnyamata wamng'ono woti amulele.

³⁴ Ndipo mu maiko uko, iwo ankadalira pa mbewu zawo. Iwo analibe zochitika monga ife tiri nazo lero, ndi—ndi mbewu zotetezera. Iwo ankadalira pa mbewu zawo. Ndipo chifukwa cha kusaweruzika kwa anthu, ndi kuvunda kwa makhalidwe awo, zinali zitabweretsa chilala pa dziko, apa iwo onse anali anjala ndi kumafa.

³⁵ Ndiyeno ife tikupeza kuti mopanda kukaika iye anali atapemphera usiku pambuyo pa usiku, usiku wonse, pamene iye amayamba kuwona kuti mbiya ya ufa inali kutsikira, tsikira, tsikira. Ndipo iyo iyenera kuti inafika pa malo mpaka kuti munali mopanda ngakhale ufa wodzaza kapu mu mtangawo. Wonse umene iye anali nawo unali wapang'ono wa m'dzanja. Imfa inali ikubwera pa chipata pomwe, pa chitseko chake. Pakuti uko kunalibe njira yowupezera wina konse. Fuko lonse linali pa njala.

³⁶ Ndipo, mafuta, anali ongodzaza mu supuni atatsala mu koikamo kakang'ono. Mafuta apang'ono pokha chotero ndi ufa wapang'ono chotero ziri pakati pa iye ndi imfa. Iye ayenera kuti anafika podzipereka kwenikweni ndi mapemphero ake. Inu mukazilola izo kuti zifike pa khomo panu, izo zidzakhala modzipereka pang'ono mopitirira kuposa momwe ife tiriri mmawa uno, pamene ife tidziwa kuti imfa ili pa khomo.

³⁷ Ndipo ine ndikukhulupirira, mwinamwake, ife tikanaganiza, mwina, ichi, kuti iye anali atapemphera utali wa usiku wonse, kwa tsiku limodzi lina zinakhazikitsa izo. Iye amakhoza kuyang'ana pa milomo yotuwa ya mnyamata wake wamng'ono wa pafupi zaka zitatatu kapena zinai zakubadwa. Ndipo iye amakhoza kuwawona mafupa ake omwe akufota, pamene mnofu unali kuchoka pa iwo. Ndipo icho chienera kuti chinali chinthu chowopsya, monga mayi uyu, powona zinthu izi zikupita. Ndipo, komabe, ndi manja ake pamaso pa Mulungu, akupemphera usana ndi usiku, "Tsopano ife tiri mpaka ku ufa wa mdzanja limodzi ndi mafuta odzaza msupuni."

³⁸ Inu mukudziwa, icho ndi chinthu chachilendo. Mulole Mulungu alowetse izi mwa mmodzi aliyense wa inu, ngati inu muti musadzandimvenso ine ndikulalikira kachiwiri. Mulole uwu ukhale uthenga. Ndi chachilendo, chachilendo kwambiri, kuti nthawi zina kuti Mulungu amachita zinthu mwanjira imeneyo.

³⁹ Inu mukudziwa, pamene ife talapa machimo athu ndi kukomana nacho chofunikira chirichonse chimene Mulungu amachifuna. . . Ife titakhulupirira pa Mulungu. Pali zochitika zimene ziyenera kuti zikomanidwe, ndipo izo ziri molingana ndi chifuniro Chake. Ndipo ife talapa machimo athu, ndipo ife takonza zolakwika zonse zimene ife tinazichita, molondola, tachita zirizonse zimene ife timadziwa kuchita kwake. Chosowekera chirichonse chimene Mulungu wapanga, kapena watifunsa, ife takomana nacho chosowekera chimenecho, ndipo komabe Iye akukhala chete. Iye sakutiyankha ife basi.

⁴⁰ Ine ndikutsimikiza kuti ine ndikuyankhula kwa anthu, mmawa uno, amene afika pa malo amenewo. Ine ndakhalapo pamene, nthawi zambiri, mwiniwanga. Pamene ine ndapita mmbuyo ndi kuwutsata moyo wanga ndi kugudubuza mwala uliwonse, ndipo ine ndikapeza kuti ndinachita chinachake cholakwika, ine ndimapita ndi kukachilapa icho ndi kuti, “Ambuye Mulungu, ine ndikachikonza icho bwino,” ndipo nkupita kukachita chomwecho. Ndiye nkubwerera kachiwiri ndi kuti, “Tsopano, Ambuye, Inu ndinu Mulungu; Inu mundiyankha ine. Ndithudi ine ndakwaniritsa chosowekera chirichonse chimene Inu munachifuna kuti ine ndichichite. Ndipo chofunikira chirichonse, ine ndachichita icho.” Ndipo komabe Iye nkusati asunthe, amawoneka kuti wangokhala duu, ndi pamene iwe uyenera kukhala uli wotsimikiza kuti Iye ndi Mulungu. Musati mukhale okhumudwitsidwa. Chinthu chokha chiri, kuti, mu mtima mwanu, kuti mukhale otsimikiza za Mulungu.

⁴¹ Mutu wanga. Khalani otsimikiza, choyamba, inu musanati muchite chirichonse. Mukhale otsimikiza, mu mtima mwanu, kuti ndi Mulungu. Ndipo pamene inu mwachita chirichonse chimene Iye ananena, ndiye inu mukutsimikiza kuti Iye ndi Mulungu, ndi pamene chikhulupiriro chimapita kukagwira ntchito, pomwepo. Chikhulupiriro chimaima njii, pakuti Icho chimadziwa kuti Iye ali.

⁴² Ndipo inu mukakwaniritsa chosowekera chirichonse. Inu mukakhulupirira kuti Iye ali, ndipo chikhulupiriro chimagwira mosasuntha. O, lodala likhale Dzina Lake! Chikhulupiriro sichiti chisunthe, pakuti icho chiri chotsimikiza kuti Mulungu ali, ndi wopereka mphoto kwa iwo amene amamufuna Iye molimbikira.

⁴³ Mulole izi zipite pansu mwakuya ndipo zisati zisunthe konse kwa inu, Branham Tabernacle. Ngati inu mwachita zofunikira

za Mulungu, ndipo mu mtima mwanu inu mukukhulupirira kuti Iye ali, Mulungu akungoyesa chikhulupiriro chanu, pakuti Iye amakonda kuchita izo. Inu mwavomereza tchimo lanu ndipo inu mwachita chosowekera chirichonse chimene Mulungu akufuna, ndipo komabe Iye nkukhala ali duu, kumbukirani, chikhulupiriro chikuti Iye ali. Ndiye chikhulupiriro chimagwiritsa kwa izo, osadziwa kuti izo zonse nzanji, koma icho chimadziwa kuti Iye ali, ndipo ndi zotsimikizika kuti Iye ali.

⁴⁴ Ndiye, kumbukirani, ngati Iye ali, Mawu Ake ayenera kukhala owona. Ndipo ngati Iye akufuna kuti inu mukomane nazo zochitika izi, ndipo inu mwatero, Iye ali wokakamizika kuti asamalire Mawu Ake. Musati mubwerere mmbuyo, ndi kuti, “Chabwino, ine sindinachiritsidwe konse. Ine. . .” O, iwe wosauka, wa chikhulupiriro chofooka. Usati uzikhulupirira izo. Ngati chirichonse chalapidwa, ndipo chirichonse chatulutsidwa, ndipo inu mwakomana ndi chofunikira cha Mulungu, chikhulupiriro chigwiritse pomwepo. Palibe chimene chiti chidzasunthe icho. Iye ali, ndipo inu muli otsimikiza. “Two amene ayembekezera pa Ambuye adzawonjezera mphamvu zawo; iwo adzakwera mmwamba ndi mapiko a mphungu. Iwo adzathamanga ndi kusakhala otopa; ngati iwo ayenda, iwo sadzakomoka.”

⁴⁵ Yembekezzerani, pamene inu mwachita chofunikira Chake. Izo zimabweretsa chikhulupiriro chanu pa chiwonetsero. Ngati inu mwachita. . . zofunikira za Mulungu zikakhala zitachitidwa, kapena kukomana nazo, ndipo inu mwazilingalira izo kwathunthu, ndipo inu mwachita chirichonse chimene Mulungu amafuna kuti inu muchite, ndiye chikhulupiriro chanu chimapuma pomwepo, kuti Iye ali. Khalani otsimikiza za Mulungu.

⁴⁶ Inu mukudziwa, Iye amakonda kuti azitiyese ife. Iye amakonda kuti aziwona zomwe chikhulupiriro chathu chiti chichite. Kodi inu mumadziwa izo? Mulungu amakonda kuwona momwe inu muti muchitire. Pamene inu munena, “O Ambuye, ine ndikukukhulupirirani Inu. Inu ndinu Mpulumutsi wanga. Ine ndikukhulupirira kuti Inu ndinu Mchiritsi. Ine ndikukhulupirira kuti Inu ndinu Mmodzi Yemwe mumapereka Mzimu Woyera. Ndi zinthu zimene ine ndiri kuzisowa, Inu ndinu Mulungu Amene mumapereka izo.” Ndiyeno pamene inu mulapa machimo anu onse ndi kumulonjeza Mulungu chimene inu muti muchite ngati Iye ati akuloleni inu kuti muchire, ndiyeno chifukwa izo siziri kuchitika, inu mumathawira kwina ngati wamantha kwinakwake. Mulungu sangakhoze kuwagwiritsa ntchito awo. Palibe njira yakuti Iye akugwiritseni inu ntchito. Palibe njira yoti Iye akuyankheni inu, chifukwa Iye amayankha mwa chikhulupiriro mokha. Ndiye, zonse mwadzidzidzi, inu mumachokapo, ndipo Iye sangakhoze

kuyankha. Koma chikhulupiro chenicheni, choona chimaima pamenepo, kukhala wotsimikiza kuti Mulungu ali. Khalani otsimikiza kuti Iye ali.

⁴⁷ Ndipo ngati Mulungu afunsa chinthu ichi kuti chichitidwe, kuti mulape machimo anu, ndi zina zotero, ndipo inu mwachita izo, chikhulupiro chimanena kuti Iye ali, icho ndi chotsimikiza kuti izo zichitika. Chopempha chanu chiyenera kuti chiperekedwe. O, ine—ine ndikuyembekeza inu simuphonya izo. Ngati inu mukutsimikiza za Mulungu, Mulungu ndi wotsimiza za Mawu Ake. Iye akungoyembekeza kuti akuyeseni inu.

Iye anachita izo nthawi zambiri. Tiyeni tibwereze nkhani imodzi kapena ziwiri.

⁴⁸ Tiyeni tiganize za ana Achihebri. Iwo sanali oti azigwadira kwa fano. Mulungu anali ndi chidaliro mwa iwo. Ndipo pamene iwo anamva kuti iwo anayenera kuti apite ku ng'anjo ya moto, iwo anati, “Mulungu wathu ali wokhoza kuti atipulumutse ife ku ng'anjo iyi. Koma ngati Iye sachita izo, ife sitigwadira ku aliwonse a mafano anu.” Mukuona, iwo anali osakaika ndi otsimikiza za Mulungu.

⁴⁹ Iwo ankadziwa kuti Iye anali Yehova. Iwo ankadziwa kuti Iye amayankha pemphero. Koma kaya Iye achita izo mu vuto lawo, kapena ayi, izo zinayenera kukhala kwa ubwino. Chotero iwo anangonena izo, analapa machimo awo, ndipo anayenda kukalowa mu imfa.

⁵⁰ Pamene iwo anali akupita ku ng'anjo ya moto, akudziwa kuti iwo anali otsimikiza, kuti, ngati Mulungu ati awalole iwo kuti apsyee, Iye akanati adzawadzutse iwo kachiwiri, mu chiwukitsiro. Iwo anali otsimikiza za Mulungu, chifukwa iwo ankadziwa kuti Mulungu akanachita chirichonse kwa ubwino wawo. Ndipo pamene ife tikhala otsimikiza za Mulungu, ife timadziwa kuti Mulungu amachita chirichonse kwa ubwino wathu.

⁵¹ Chotero, iwo anapanga kunena kumodzi. Iwo anali otsimikiza, ndipo iwo anayenda mpaka mu ng'anjo yamoto. Ndipo Mulungu anawalola iwo kuti apite kumeneko; atakhala, akuyang'ana pa iwo. Iye ankafuna kuti awone momwe iwo akanachitira.

⁵² Pamene, mfumu inati, “Kodi inu munagwada pamene lipenga linawomba?”

Iwo anati, “Ayi. Ife sitinagwade.” Apo pali chikhulupiro chanu, chitagwira molimba.

“Chabwino, ndiye, ngati inu simunagwade, inu mukudziwa kulamula kwanga.”

“Inde, ife tikudziwa kulamula kwanu.”

“Kulamula kwanga ndi kwakuti ng’ango itenthetsedwa kasanu ndi kawiri kutentherapo kuposa momwe inayamba yakhalirapo, ndipo ine ndikuponyerani inu mkati mmenemo. Kodi tsopano inu mukufuna kuti mugwade?”

“Ayi. Ife sitigwada ayi.” Apo pali chikhulupiriro chawo.

⁵³ Mulungu akuti, “Chabwino, ine ndiwona chimene iwo ati achite pa icho. Ine ndiwona kuchita komwe chikhulupiriro chawo chiri nako.”

⁵⁴ Chotero iye anati, “Mangani manja awo, ndipo mumange mapazi awo, ndipo apititseni iwo ku ng’ango.” Ndipo iwo anayenda mpaka ku ng’ango imeneyo, ali ndi moto mu nkhope zawo. Mulungu ataimabe, akuyang’ana pa izo. Koma iwo anali otsimikiza kuti Iye anali Mulungu. Iwo anali atapanga kulapa kwawo. Iwo anali atakonzza chirichonse molondola, chimene iwo ankachidziwa. Iwo anali otsimikiza kuti Iye anali Mulungu.

⁵⁵ Chotero iwo anayenda mpaka ku ng’ango ya moto imeneyo. Mpaka pa mphindi yotsiriza, pamene Iye anabwera atakwera kuchokera mmiyamba, pa galeta wa mphepo, anakupizira mphepo pa iwo, pamene Iye anali kuwatonthoza iwo ndi kuyankhula kwa iwo.

⁵⁶ Mulungu amalola kuti chikhulupiriro chako chifike pa malo pamene icho chingachitepo.

⁵⁷ Kunali Yobu, wa Chipangano Chakale, pamene Satana, wotitsutsa wathu, anamutsutsa iye za kukhala wochimwa mwa mseri. Koma Yobu ankadziwa kuti iye anali asanachimwe. Iye ankadziwa kuti iye anali atalapa chirichonse chimene iye anali atachita, ndipo anali ataika chopereka chopsyereza kunja uko. Icho chinali chofunikira cha Mulungu. Ndizo zonse zimene Mulungu ankafuna, chinali chopereka chopsyereza chija ndi kuvomereza. Ndipo Yobu anali atachita zinthu zimenezo.

⁵⁸ Ndipo Satana anati, “Ine nditenga ngamira zake, pakuti iye ndi munthu wolemera. Ine nditenga nkhosha zake.” Ndipo potsiriza iye anamutengera ana ake, chapafupifupi kwa mtima wake.

⁵⁹ Komabe, Yobu anaima nji, pakuti iye ankamudziwa Mulungu ameneyo. Chabwino, iye anali wotsimikiza kuti Iye anali Mulungu, pakuti iye anali atayankhula ndi Iye, ndipo iye anali atachita zofunikira Zake. Iye anafufuza ndipo anapeza, “Ine ndapanga chopereka chopyereza chirichonse. Ine ndinati mu mtima mwanga, Mwinamwake pamene ana anga apereka—phwando, ndipo ana anga aakazi analiko, mwina iwo anakachita mwamseri tchimo mu mtima mwawo, chotero ine ndipereka chopereka chopyereza kwa iwo ndi kuvomereza cholakwitsa chawo.”

⁶⁰ O Mulungu! Pamene munthu asunga zimene Mulungu ananena kuti achite, iye amakhala wotsimikiza kuti Iye

ndi Mulungu, Iye ayenera kuti ayankhe. Chikhulupiriro chimamuitanira Iye powonekera, nthawi iliyonse.

⁶¹ Pamene iwe wachita chimene iwe ukudziwa kuti chinali cholondola, pamene iwe wakomana ndi zofunikira Zake, pamene iwe wavomereza ndi kukonza molondola, ndi kukonza zolakwika, ndi kuziyika izo pamaso pa Mulungu. Ine sindikusamala kaya Iye ali chete motani, Iye akadali Mulungu, akudikira kuti ayike chikhulupiriro icho pamenepo. Inu mwachita ntchito zanu, tsopano Iye akufuna kuti awone chikhulupiriro chanu mwa ntchito zanu. Iye akufuna kuti awone chimene inu muti muchite.

⁶² Ngati inu mwadzozedwa ndi kupemphereredwa, Mulungu akudikira kuti awone chimene inu muti mukhulupirire za izo. Osati kuthamangira Lamlungu lotsatira, ndi kuthamanga tsiku lotsatira, ndipo akabwera wochiritsa wina mu mzindawo. Iye akuyembekeza kuti awone mmene mutachitire pa chikhulupiriro chanu. Osati kubwerera mmbuyo, tsiku lotsatira, ndi kuti, “Ine ndikumverera moyipa kwambiri, ine sindikuganiza kuti ine ndachiritsidwa.” Inu simuli oyenera ku mzere wa pemphero, pa malo oyamba. Inu simuli. Inu simuli. Inu simuli okonzeka, apo. Inu simuli kukhulupirira kuti Iye ndi Mulungu. Ine sindikutero . . .

⁶³ Inu mukhoza kunena kuti, “M’bale Branham, ine sindikugwirizana nanu inu.” Zochita zanu zomwe zikutsimikizira chimene inu muli. “Ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo.” Munthu kumati iye ndi Mkhristu; ndipo iye akumamwabe, ndi kumasuta, ndi kumachita njuga, ndi kumanena nthabwala zoyipa, ndi kumati, “Gawo la Baibulo ndi lolondola, ndipo magawo ena ayi.” Iye akhoza kumalalikira Uthenga, ndi kumakana gawo la Baibulo. Iye akadali wochimwabe. Iye sali molondola, apo.

⁶⁴ Koma pamene inu munena mwapoyera kuti Mulungu ali yemweyo Mulungu, ndipo moyo wanu nkukhala mu manja Ake, kuti, “Ambuye, ine ndine dongo; Inu ndinu Wowumba,” ndiye mupempe chimene inu mukufuna. Chikhulupiriro sichidzasuntha konse. Icho chidzaima apo pomwe.

⁶⁵ Ngakhale zochitika zitawoneka kuti zikugwera kumanja ndi kumanzere, koma chikhulupiriro icho sichingasunthe konse, chifukwa iwe uli wotsimikiza kuti Iye ndi Mulungu. Ndipo ngati Iye ali Mulungu, Iye amasunga lonjezo Lake. Iye sangakhoze kupanga lonjezo ndi kuliswa ilo. Ngati Iye ali Mulungu, Iye ayenera kuti asunge lonjezo Lake. O, ine ndimakonda izo. Iye ayenera kukhala nalobe ilo.

⁶⁶ Yobu anapanga zopereka zake; iye anachita chirichonse. Iye ankadziwa kuti iye anali kulondola. Ndipo apa panabwera mamembala a mpingo, ina ya mpingo ya zipembedzo zina, anati, “Yobu, inu mukhoza kungovomerezanso kuti ndinu wochimwa,

pakuti Mulungu sangakuloleni inu kuti mulangidwe monga chonchi kupatula ngati inu mukanakhala wochimwa.”

⁶⁷ Koma Yobu anati, “Ine ndapanga kuvomereza kwanga. Ine ndayika chopereka chopyereza pamaso pa Mulungu, ndipo ine sindine wochimwa.” Iye ankadziwa pamene iye anali kuima. Ndiye chirichonse chinkapitirira, kumangomapitirira ndi kupitirira ndi kupitirira, molimba basi monga izo zikanamakhoza kupitira, kuyesera kumuika Yobu pansu, ndi kumubweretsa Yobu pa malo pamene iye akadamukana Mulungu ndi kukana chopereka chopyereza chiya. Miniti yomwe pamene iwe ungachite pa chirichonse chimene iwe ukuchivomereza, izo zimasonyeza kufooka kwako, kumukaikira kwako Mulungu. Iwe ukamupempha chirichonse Mulungu, ndi kumapita mozungulira ukuchikayikira icho, ndiye ndiwe wokaikira ndipo osati wokhulupirira.

⁶⁸ Yobu ankadziwa pamene iye anaima, ndipo iye anaima zolimba pa maziko amenewo.

⁶⁹ Palibe zodabwitsa Pruitt anati, mu ora lake lakufa:

Pa Khristu, Thanthwe lolimba, ine ndaima;

Maziko ena onse ndi mchenga wotitimira.

⁷⁰ Pa thanthwe lolimba lija la kuvomereza kwa Yobu, ngakhale mkazi wake wokondedwa anayenda kutuluka. Pamene thanzi lake linali litapita, ndipo zotupa zinali ziri paliponse pa iye, ndipo iye anadzikhula yekha ndipo anatemberera tsiku limene iye anabadwa. Anati, “Mulole dzuwa lisawale nkomwe! Mwezi ukhale utalowa usiku.”

Mkazi wake anati, “Yobu, ndiwe womvetsa chisoni kwambiri. Bwanji iwe sukumutemberera Mulungu ndi kufa?”

⁷¹ Iye anati, “Iwe ukuyankhula ngati akazi opusa.” Iye anali wotsimikiza kuti kunali Mulungu, ndipo iye anali atachita zofunikira. O, ine ndikumverera mwachipembedzo. Iye ankadziwa kuti iye anali atakomana ndi zofunikira za Mulungu, ndipo izo zikukhazikitsa icho. Mulungu anali akuyesa chikhulupiriro chake. Iye adzayesa chanu. Iye adzayesa changa.

⁷² Koma pamene ife tachita zofunikira Zake, “Lapani mmodzi aliyense wa inu ndipo mukhale obatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha machimo anu, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera,” ndilo lonjezo Lake. “Alipo aliyense pakati panu akudwala, kayitaneni akulu a mpingo. Mulole iwo awadoze iwo ndi mafuta, ndi kuwapempherera. Pemphero la chikhulupiriro lidzapulumutsa wodwala, ndipo Mulungu adzawadzutsa iwo.” Izo zikukhazikitsa icho. “Vomerezani zolakwa zanu, wina kwa mzake, ndipo pemphereranani wina kwa mzake.” Inu mwachita zofunikira za Mulungu.

⁷³ “Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira. Mu Dzina Langa iwo adzatulutsa ziwanda; iwo adzayankhula ndi lirime latsopano; ngati iwo atenga njoka kapena kumwa zinthu zakupha, izo sizidzawapweteka iwo; ngati iwo ayika manja awo pa odwala, iwo adzachira.” Izo zikukhazikitsa icho.

⁷⁴ Khalani otsimikiza za Mulungu. Tsimikizani, izo mu mtima mwanu, kuti inu mukukhulupirira kuti awo ndi Mawu a Mulungu. Yobu anali.

Mkazi wake anati, “Bwanji inu simukumutemberera Iye ndi kufa? Bwanji, inu mukupeza moyipirabe nthawizonse.”

⁷⁵ Momwe Satana amakondera kuonyera izo pa iwe. “Bwanji, inu simuli bwinoko kuposa momwe inu munali pamene inu mumadzozedwa. Inu simuli bwinoko kuposa pamene alaliki aja anakupemphererani inu. Alaliki aja sali kulondola, mmalo oyamba.” Izo ziribe kanthu za mlaliki uja. Ndi chikhulupiriro chanu mwa Mulungu wamoyo, zimene zimawerengedwa. Osati chimene mlaliki ali; ndi chimene Mulungu ali. Mlaliki sanapange konse lonjezo; Mulungu anapanga lonjezo. Siziri kwa mlaliki; izo ziri kwa Mulungu, ndipo chikhulupiriro chanu ndi choti chikhulupirire kuti uyo ndi Mulungu. Chotero khalani otsimikiza za Mulungu. Khalani otsimikiza kuti ndi Mulungu, ndipo awo ndi Mawu a Mulungu. Ndipo Mulungu ali mu Mawu Ake.

⁷⁶ Ndipo Yobu anati. “Iwe ukuyankhula ngati mkazi wopusa.” Anati, “Ambuye anapereka, ndipo Ambuye atenga; lodala likhale Dzina la Ambuye.” Iye anali wotsimikiza kuti analipo Mulungu.

⁷⁷ Ndipo pamene iye ananena izo kuchokera mkamwa mwake, mabingu anayamba kubingula ndipo mphezi zinayamba kung’anima. Mulungu anasunthira powonekera. Izo nthawizonse zimamuitanira Iye powonekera. Iye anakhala chete kwa nthawi yaitali.

⁷⁸ Ndicho chimene Iye akuchita. Tayang’anani pa gulu ili la Achimereka lopita ku gehena, achinyengo opita ku tchalitchi. Ine sindinakwiye. Koma tchimo limamukwiyitsa wina aliyense yemwe ali woyanjana ndi Mulungu. Sikuti ndakwiya nalo fukoli, sikuti ndakwiya nawo anthuwa, koma ine ndakwiya naye Mdierekezi yemwe wayambitsa zinthu izi kuti ziwachititse khungu anthu.

⁷⁹ Azibusa akhungu awa ndi azilaliki kuwalola iwo azidutsa nazo ndi zamulungu zina pang’ono zopangidwa ndi anthu. Iwe uyenera kuti ubadwe kachiwiri. Ndipo Mulungu amasunga Mawu Ake. Ndikumuwona iye pamene iye akuwakhazika iwo chete. Iwe uyenera kukhala wotsimikiza kuti alipo Mulungu. “Okhala nawo mawonekedwe aumulungu, ndi kumakana Mphamvu yake.”

⁸⁰ Mkazi wosauka, wamng'ono uyu, iye ankadziwa kuti Iye anali Mulungu. Pamene mbiya iyo inali kutsikira, pansi, pansi, pansi, zinthu zimaipira yipira, nthawi zonse. Koma Mulungu amazilola izo kuti zifike mwanjira imeneyo. Iye amangokonda kuchita izo. Iye amakonda kuyika chikhulupiriro chako poti chiyesedwe, kuti awone momwe iwe uti uchitirepo pa izo, amakulola iwe kuti udzozedwe ndi kupemphereredwa, ndiye nkukupangitsa iwe kudwalika. Anati, “Tiyeko, Satana, kamuyike iye poyesedwa. Ine ndikudziwa kuti iye akundikhulupirira Ine.” Mulungu adalitsidwe kwanthawizonse! O, mai! [M'bale Branham akuwombetsa manja ake kawiri—Mkonzi.] “Anamuika iye poti ayosedwe tsopano. Ine ndikudziwa kuti iye anatenga Mawu Anga pa izo.” Kodi Iye anganene izo pokamba za inu?

⁸¹ Iye ananena izo pokamba za Yobu. Anati, “Chita chirichonse kwa iye chimene iwe ukufuna kuchita, koma iwe usati utenge moyo wake, chifukwa ine ndikudziwa kuti iye amandikonda Ine. Iye wapanga nsembe yopyereza. Iye wapanga zofunikira. Iye wachita zimene Ine ndinamuuza iye kuti azichita, ndipo iye akuzikhulupirira izo. Tsopano mugudubuze iye pa makala ngati iwe ukufuna kuti utero.” Iye anachotsa chirichonse kutali ndi iye. Mulungu anawirikiza izo pamene Iye ankaperekanso izo kwa iye. Zedi, Iye adzatero.

⁸² Iye amaika chikhulupiriro chathu poti chiyesedwe, kuti awone ngati ife timakhulupirira kwenikweni kuti Iye ndi Mulungu.

⁸³ Mkazi wamng'ono uja, mopanda kukaika, anati, “Ine ndinapemphera. Ine ndinapemphera. Ine ndikudziwa kuti ndine Wamitundu wosayenera.”

⁸⁴ Kumbukirani, Yesu anayankhula za iye mu Baibulo. Iye anati, “Kodi simunali akazi amasiye ambiri mu masiku a Eliya? Koma iye anatumizidwa kwa mmodzi yekha, ndipo iye anali Wamitundu.”

⁸⁵ “O,” iye anati, “Ine ndikupemphera.” Mwinamwake, pamene iye anawona mkate wotsiriza wawung'ono uja, imfa inali italowa kale pa chipata ndipo itabwera kudzalowa pakhomo. Kuluma kumodzi kwina, mbamu, ndipo iye ndi mwana wake akanafa. Ine ndikukhoza kumuwona iye, usiku wonse, akupemphera, mphepo zotentha zija zikupemerera, ndipo dziko litawawuka, ndipo anthu akulira ndi kufuula mu misewu. Iye anayenda mozungulira, kudutsa mnyumbamo. Iye anayang'ana pa mwana wake wamng'ono. Anayang'ana pa zovala zake zogonera zazing'ono; izo zonse zinali zosamukwana, ndipo mapazi ake atatulukira kunjira. Anayang'ana pa manja ake omwe, atakhwinyata. Iye anayenda mmbuyo ndi mtsogolo, koma iye anati, “Ine ndikudziwa kuti Iye ndi Mulungu. Ine ndapanga kulapa kwanga konse. Ine ndachita chirichonse

chimene Iye amafuna. Ine ndikupempha kufunira miyoyo yathu, kwa ulemerero Wake.” Mulungu anamuwona iye.

⁸⁶ Onse a iwo anali akupita kunja ndi kumakakhala ndi kuvina kwakukulu kwinakwake, akumadzikongoletsa okha, akumakakhala ndi kuwonetsa televizioni kwamakono kapena chinachake, kumapitirira ndi dziko. Koma mkazi uyo anali yekha ndi Mulungu.

⁸⁷ Kuwala kwa tsiku kunatulukira. Iye anati, “Mwanayu walira utali wa usiku wonse, kuti adye chinachake. Ine ndichita chiyani ndi ufa wapang’ono wokwanira mdzanja?”

⁸⁸ Inu mukudziwa, ufa umenewo unali Khristu. Wophunzira aliyense wa Baibulo amadziwa kuti Khristu anali nsembe ya Ufa. Ndipo nsembe ya ufa iyo inkayenera kuti iperedwe ndi choperera chapadera, nachonso, kufikira icho chitadula chidutswa chaching’ono chirichonse cha chimanga mofanana; chifukwa Yesu Khristu ali yemweyo, dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndipo wokhulupirira aliyense amakhulupirira izo ndipo amapuma pa izo. Aleluya! Inu mukhoza kukhala nacho chipembedzo chanu chakale, chozizira chofunda chimene inu mukuchifuna. Kwa ine, ine ndikukhulupirira Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ine ndikupanga kuima kwanga mu dziko la achikunja. Ine ndikukhulupirirabe kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

⁸⁹ Zoperera zimenezozitadula chidutswa chirichonse cha iwo mofanana basi, chifukwa Iye ali yemweyo. Iye ali Mulungu yemweyo yemwe anali panthawiyo, Iye ali pakali pano, mmawa uno. Iye nthawizonse adzakhala ali yemweyo. Ndicho chimene ufa unkatanthauza.

⁹⁰ Ndipo mafuta amatanthauza Mzimu, monga ife tikudziwira molingana ndi Ezekieli 4, ndi zina zotero. Ndicho chifukwa ife timadzoza ndi mafuta; ndi Mzimu. Ndi chiyani icho? Monga Yohane Woyera 4, “Atate amafuna otero kuti azimupembedza Iye mu Mzimu ndi mu Choonadi.” Yesu anali Choonadi. Iye anali nsembe ya Ufa, ndipo mafuta awa anali Mzimu. Ndipo Mzimu, ukasakanizikana ndi Choonadi, izo ziyenera kupereka chinachake. Mukaziyika izo palimodzi, izo zimapanga keke. O!

⁹¹ Chikhulupiriro chanu chiri kuti? Pamene Mawu a Mulungu akulalikidwa mu kuphweka Kwake, ngakhale mu Mphamvu Yake, kuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, ndipo Mawu amapita chifukwa cha Ufa, inu muli ndi Mafuta kuti musakanize ndi Iwo. Iwo mwina akhoza kungokhala amdzanja, kapena amsupuni, koma, chirichonse chimene iwo ali, ndi chenicheni.

⁹² Tsopano izo zikukonzekera chiyani? Izo zikukonzekera mtanda. Izo zikukonzekera nsembe-yayekha. Ndicho chimene iwe uyenera kuchita. Ngati Mawu alalikidwa, ndipo iwe ukakhala nawo Mzimu ndi Iwo zitasakanizidwa palimodzi,

ndi nsembe-yawekha kuti ukane kupweteka kulikonse, kuti ukane matenda aliwonse, kuti ukane chirichonse chimene chiri chosiyana ndi Mawu a Mulungu, ndi kuima pa icho.

⁹³ Adokotala akunena *izi, izo*, kapena *china*; sizimapanga pang'ono pa kusiyana. Iwe umayima pa Icho, chifukwa Mulungu ananena chomwecho. Ufa wabwera. Inu muli ndi Mafuta. Inu mwazisakaniza Izo palimodzi.

⁹⁴ Tsopano, ine ndikumva liwu. Ndi pang'ono kuwala kwa tsiku kutadza. Liwu likuyankhula, ndi kuti, “Pita panja kuseri ndipo ukatenge nkhuni ziwiri.” Kodi inu munazindikira, Lemba linati “nkhuni ziwiri”? Mtanda. Iye ali ndi ufa ndi mafuta, koma iye akuti ayitanidwe, kuti achitepo tsopano; achitepo ndi izo. Kaya ndi zochulukwa bwanji uli nazo, Ufa wochulukwa kapena Mafuta monga iwe ukanawasowera, koma iwe uyenera kuchitapo; nsembe-yawekha.

⁹⁵ Nkhuni ziwiri. Mu nthawi yakale iwo sankapeza konse njira yabwinopo kuti ukoleze moto. Pamene iwe utenga nkhuni ndi kuigoneka iyo chopingasa nkhuni, kuyatsa iwo pakati, iwe umasonkhezera mapeto onse. Momwe amwenye amayatsira moto wawo. Ine ndayatsapo iwo, nthawi zambiri, utali wa usiku wonse. Kungotenga chipika, ndipo icho mwanjira *iyi*, ndi chinacho mwanjira *iyoyi*, ndi kumangopitirira kuchikankhira icho mmoto pamene icho chikuyaka.

⁹⁶ Nkhuni zimenezo zinali mtanda. “Nkhuni ziwiri,” Baibulo linatero. Liwu linati, “Pita kudutsa kuseri ndipo ukatole nkhuni ziwiri.” Nthawi yomweyo, pa phiri, uko kunali liwu linabingulira pansu kwa mneneri ndipo linati, “Pita ku mzinda. Ine ndamulamulira.” O, mai! Onse a iwo anamvera. Chinachake chiyenera kuti chichitike. Onse a iwo akumvera.

⁹⁷ Ngati mlaliki alalikira Mawu, ndipo munthu yemwe awalandira Iwo akawakhulupirira Iwo ndi kuchitapo pa Iwo, chinachake chiyenera kuti chichitike. Ngati ndiwe wochimwa, iwe uyenera kuti upulumutsidwe. Ngati iwe ukudwala, iwe uyenera kuti uchiritsidwe, chifukwa Mulungu analonjeza izo, ngati ife tiri otsimikiza za Mulungu.

⁹⁸ Motsimikiza monga Iye ali Mulungu, Iye ayenera kuti azisunga Mawu Ake. Ndithudi! Ndiye kulamulira kunali, “Pita ku mzinda, pakuti Ine ndamulamulira mkazi wamasije.” Masomphenya anatseguka pamaso pa mneneri. Apa iye akubwera, akuyenda. Iye sakudziwa kumene iye akupita; izo sizimapangitsa kusiyana kulikonse. Iye akungomvera.

⁹⁹ Mkaziyo sakudziwa kumene nkhunizo ziti zikhale ziri, koma kuli nkhuni ziwiri kuseri penapake. Iye akuwuyamba. Iye akupita panja kuseri. Iye akuyang'ana pozungulira, “O, kwatentha bwanji!” Kufuula kochokera ku mzinda, oyendayenda usiku akubwera kumeneko, akumenyenirana kumeneko, akumwa vinyo wawo, ndi zina zotero. Iye

akuyang'ana pansi mu msewu. Iye sakuwona kanthu. Iye akupeza nkhuni imodzi; gawo la mtanda, nsembe-yayekha. Iye akutenga chidutswa china, nkhuni. Ndipo pamene iye anatola nkhuni yachiwiri iyo. . .

¹⁰⁰ O, iko kuyenera kuti kunali kolunda bwanji, imfa itagona pa khomo. Iye ndi mwana wake anali oti adye chidutswa chimodzi chaching'ono cha mkate ndi kufa. Izo zinali zonse za izo. Ndipo nthawizina, mkati momwe mwa kulunda, ndi mmene ife timalimva liwu.

¹⁰¹ Pamene iye anaitola nkhuni yachiwiri iyo ndipo atayamba kubwerera, apo panali liwu limene linabwera pamwamba pa chipata, linati, "Kanditengere ine madzi pang'ono mu chikho."

¹⁰² Iye anapotoloka kuti awone, ali ndi nkhuni ziwiri izi mu dzanja lake, ali ndi ufa ndi mafuta zitasakanizidwa ndipo atakonzeka. Iye anati iye anali atakonza izo, atasakaniza izo palimodzi. Ndicho chimene, Mawu ndi Mzimu, ziyenera kusakanizana limodzi. Kuikidwa pa mtanda wa kudzipereka-nsembe, kuti uzikana chirichonse chimene chiri chosiyana ndi chimene iwe wapempha. Ndiko kulondola. "Ine ndasakaniza izo, tsopano ine ndikupita kukatola nkhuni izo."

Ndipo liwu lija linati, "Ndibweretsere ine madzi akumwa pang'ono, mu chikho."

¹⁰³ Iye akuyang'ana, ndipo iye akuwona mwamuna atayima, atatsamira pa chipata, wa matsaya-owonda, wamasharubu, mutu wadazi, akuyang'ana chaku chipata, ali ndi chidutswa chaching'ono cha chikopa cha nkhusa chitakulungizidwa pa iye. Ankawoneka ngati iye anali ngati bambo waulemu wachikulire wowoneka-wachifundo.

¹⁰⁴ Iye anati, "Ine ndigawana madzi anga ndi iye." Madzi a Moyo, inu muli lolera kuti muwapereke iwo kwa wina aliyense, kuti mumuwuze aliyense, kuti apite kulikonse. "Mphindi chabe, bwana." Iye akuyamba kubwerera, ali ndi nkhuni mdzanja lake.

¹⁰⁵ Ndipo liwu linabingula kachiwiri, "Osati kokha kuti undigawire madzi ako, koma undibweretsere ine chidutswa chaching'ono cha mkate mu dzanja lako." Mkate wa moyo; madzi a moyo! Kodi iwo unali wa moyo? Iye akanafa posakhalitsa pamene izo zikanatha. "Undibweretsere ine madzi ako ndipo undibweretsere ine mkate wako."

¹⁰⁶ Kodi ife tikupeza chiyani apa? Ndi phunziro lotani limene ife tingakhoze kulipeza? "Funani inu poyamba Ufumu wa Mulungu, ndi chilungamo Chake chonse; zinthu zina zidzawonjezedwa."

"Ndibweretsere ine madzi pang'ono ndi mbamu ya mkate."

¹⁰⁷ Ndiye iye akutembenuka, mwa kulunda kwake. Ine ndikukhoza kumumva iye akuti, "Bwana," chinachake chonga ichi, "ndinu wosiyana ndi amuna amene ine ndawawonapo, ndi amuna amene ine ndimawamva akuyankhula. Inu mukuoneka

kuti ndinu wotsimikiza kwambiri pa chimene inu mukunena. Koma ine ndangokhala ndi ufa wokwanira, wamdzanja wokha, ndi mafuta amsupuni okha. Ine ndazikonza izo, ndipo ine ndikupita kuti ndikaziphike izo ndi nkhu ziwiri izi. Ndipo ine ndikuti ndidye izo, ine ndi mwana wanga, ndipo tifa. Ndi zonse zimene ine ndiri nazo.”

108 Ife tikumva chiyani, ndiye, motsatira? “Koma, kanditengere ine mkate waung’ono, choyamba.” Mulungu, choyamba. Ziribe kanthu zimene wina anena, chimene chirichonse, umboni uliwonse, kaya izo zikuwoneka zolunda motani, chirichonse chimene icho chingakhale chiri, mutengeni Mulungu, poyamba. Mawu Ake, choyamba.

109 “Adokotala anati ine sindingakhoze kukhala bwino.” Koma, Mawu Ake, choyamba. “Ndine wochimwa mochuluka kwambiri. Ndine wachiwerewere. Ndine wajuga. Ndine chidakhwa.”

Mawu a Mulungu, choyamba. “Ngakhale machimo anu atakhala ofiira, iwo adzakhala oyera monga chipale; ofiira monga kapezi, iwo adzakhala oyera monga ubweya.” choyamba, Mulungu.

110 “Pita, kandibweretsere ine mkate waung’ono, choyamba. Zonse zimene iwe uli nazo, kazibweretse izo kwa ine.” Kodi ndiwe wololera kuti uzipereke izo mmanja Mwake?

111 Moyo wanga, zonse zimene ine ndiri. Ndine wausinkhu wa zaka makumi asanu. “Kodi iwe ukulolera, William Branham, kuti uzipereke izo kwa Ine? Kodi inu mukulolera, inu ana aang’ono, kuti mupereke moyo wanu kwa Ine? Kodi inu mukulolera? Kodi inu mungakhoze kuchita izo, anthu odwala? Kodi inu mungakhoze kundidalira Ine? Ndiyikeni Ine poyamba.”

112 “Kandibweretsere ine mbamu ya mkate mdzanja lako, ndipo kanditengere ine madzi pang’ono.” Iye anayang’ana pa iye. Apo panali chinachake chimene chinamuza iye kuti bambo ameneyo akudziwa za chimene iye akuchinena.

Mulungu amadziwa nkhusa Zake Zomwe. “Nkhusa Zanga zimadziwa Liwu Langa. Izo zimadziwa ngati ilo liri Lemba kapena ayi, ngati ilo liri kulondola kapena ayi.”

113 Iye akupotoloka, mwa kumvera. Ndicho chimene inu muyenera kuti muzichita. Ndipo pamene iye anapotoloka, kuti amvere chimene mneneri ananena kuti achite, ndiye panabwera bingu kuchokera Kumwamba, lomwe munthu aliyense amayang’anira kuti alimve. Pakuti, apo panabwera bingu kuchokera mliwu la mneneri, limene wochimwa aliyense ndi munthu wodwala aliyense amakhumba kuti alimve, “PAKUTI ATERO AMBUYE.”

114 Momwe ife timakhumbira kuti tilimve Ilo! Momwe kuti anthu amakhala mu njira yanga, ndi kuti, “Bwerani ku khomo ili. Mwana wanga wamkazi ali *motere*. Khanda langa, langa,

motsika kwambiri. Mukangonena mawu.” Iwe unganene motani iwo asanakhale mkamwa mwako? Iwe ungakhale ukuwanena iwo iwemwini. Koma iwo akuyembekeza kuti awamve iwo, “PAKUTI ATERO AMBUYE.”

¹¹⁵ Apo ilo linadza, kuseri kwa mpanda, chifukwa iye anali kumvera. Ndipo kulunda kunasweka. “PAKUTI ATERO AMBUYE. Mbiya siyiphwera, kapena nsupa kuwuma, mpaka tsiku limene Ambuye Mulungu adzatumiza mvula pa dziko lapansi.” O, ndi chithonhozo bwanji!

¹¹⁶ Iye anapanga mkate. Iye anawupereka iwo kwa mneneri. Iye anabwerera ndipo anakamupangira wina mwana wake ndi wa iyemwini. Ndipo iwo anadya ndi kumwera, ndi zochuluka, pa dziko lapansi.

¹¹⁷ Kodi izo zinachokera kuti? Kodi izo zinafika motani kumeneko? Mwasayansi mudiuze ine kumene ufa umenewo unachokera. Kodi mafuta amenewo ankachokera kuti? Kodi iwo anafika chotani mu nsupa imeneyo? Iye anali akutsanulamo iwo, mmawa uliwonse. Iye amakhuthula mbiya ya ufa, mmawa uliwonse, ndipo umo munali mowuma. Koma pamene iye ankabwerera kuti akatenge wina, iwo unali mmenemo. Kodi iwo unachokera kuti? Mutengeni Mulungu pa Mawu Ake. Khalani otsimikiza za Mulungu. Iye ndi Mlengi.

¹¹⁸ Inu mukhoza kukhala kuti mwataya thanzi lanu. Inu mukhoza kukhala kuti mwataya chiyanjano chanu. Mutengeni Iye pa Mawu Ake. Khalani otsimikiza kuti Iye ndi Mulungu. Nthawi zolunda zimene zikuwoneka tsopano, zikhoza kusawoneka zolunda kwambiri ngati inu mutangotenga Mawu Ake ndi kukhala otsimikiza kuti Iye ndi Mulungu.

¹¹⁹ Mu Germany, kamodzi, ine ndinawona chithunzi, ndipo icho nthawizonse chimandikanirira ine. Wojambula wachi German anajambula... chithunzi chimene—chimene chimatchedwa “Dziko la Mtambo.” Ndipo pamene iwe uchipenya icho, uli cha patali, icho ndi kulunda kowoneka-mowopsya kumene iwe unayamba wakuwonapo. Kungokhala mitambo itaundana pamodzi, pamene iwe ukuyang’ana pa icho kuchokera pa mtunda wautali. Koma pamene iwe uyamba kuyandikira kwenikweni kwa icho, icho chimasintha. Ndi mapiko a Angelo akuwombetsa pamodzi, akuimba maaleluya kwa Ambuye. Chotero ndicho chimene kulunda kuli nthawizina. Ngati inu mukuyang’ana pa iko, pa mtunda wautali, izo zimawoneka zolunda ndi zamdima. Koma mukamutenga Mulungu pa Mawu Ake ndi kukhala otsimikiza kuti Iye ndi Mulungu, ndi kusunthira pafupi kwa icho inu mudzapeza kuti ndi mapiko chabe a Angelo akukupiza limodzi.

¹²⁰ Iye anali china monga Abrahamu anali, woitanidwa kuti apereke chirichonse chimene iye anali nacho, kuti achiyike icho pa guwa la nsembe. Mwina inu mwaitanidwa monga choncho,

mmawa uno. Siyani njira zanu. Siyani kusakhulupirira kwanu. Siyani chirichonse chimene inu muli nacho. Ndiyeno mutenge Mafuta ndi Mawu, ndipo muzisakanize Izo limodzi, ndipo muziyike Izo pa guwa la nsembe-yawekha. Inu mudzapeza, Izo zidzaitana Mulungu powonekera, motsimikiza monga ine ndaima mu guwa lino.

Ziganizani za izo pamene ife tikupemphera.

121 Kodi inu muli ndi chosowa lero? Kodi inu muli ndi chosowa chachikulu kuposa momwe inu muliri okhoza mwathupi kuti muchipeze? Kodi ndalama nzochepea chotero mwakuti inu simungakhoze kulipira lendi yanu? Kodi ana akufuna nsapato zatsopano, ndipo inu mulibe ndalama zoti mugulire izo? Kodi m'mbiya ndi mopanda kanthu kunyumba kwanu, ndipo mu msupa muli pafupi kuti mukhale mowuma? Inu mukulephera kuti mugule zakudya za ziweto zanu? Ndipo, uko, chinachake chavuta? Kumbukirani, Iye anapanga lonjezo.

122 Kodi inu mukudwala, ndipo adokotala ati inu mukusowa opareshoni? Kodi inu mulibe ndalama zoti muchitire izo? Muli ndi chosowa.

123 Kodi ndinu wochimwa? Kodi chosowa chanu ndi chachikulu, kudziwa ngati Mulungu atati aitane, lero, inu mukanati mukhale otayika? Kodi ndinu wobwerera mmbuyo mukuthawa kwa Mulungu? Ndipo inu mukudziwa kuti ndinu wa mpingo wina, koma inu mukudziwa kuti inu simuli bwino? Chikumbumtima chanu chomwe chikukuuzani inu, molingana ndi Mawu, kuti simuli mwabwino. Ndipo inu muli ndi chosowa. Musati mulole mawu awa agwere mu nthaka yaminga, kapena pa miyala, mitima yamiyala. Mulole iwo agwere mu nthaka yabwino, yachonde.

124 Ngati inu mukudwala ndipo inu...adokotala akuti inu simungakhoze kupeza bwino, ndipo inu mukumulonjeza Mulungu kuti inu mumutumikira Iye masiku onse a moyo wanu, ndipo ndinu wotsimikiza kuti Iye ndi Mulungu, bwerani mudzakomane ndi chofunikira Chake. Ngati inu muli ndi chosowa, kodi inu mungati choyamba muchite mochuluka monga kukweza dzanja lanu kwa Mulungu, kuti inu muli ndi chosowa cha chinthu china? Mulungu akudalitseni inu.

Tiyeni ife tipemphere.

125 O Ambuye, motsimikiza basi monga ine ndiriri mu guwa ili mmawa uno, ine ndikudziwa kuti sipakanakhoza kukhala limodzi la manja amenewo litapita mmwamba wopanda Inu kudziwa za ilo, pakuti Inu ndinu Mulungu. Inu munati, "Kodi mpheta zambiri sizimagulitsidwa ndi makobiri awiri? Ndinu ochuluka bwanji kuposa mpheta!" Ndi ochuluka bwanji manja amene Inu munawona a anthu achivundu awo, omwe Mwana Wanu Yesu anawafera! Ndi momwe Inu mukanachitira mochuluka kuwaona manja awo kuposa momwe

Inu mukanachitira kwa mpheta, ngati iyo ikanagwa mmawa uno! Ine ndikulingalira, kuti mpheta khumi ndi ziwiri, sizikanati zigulitsidwe kobiri mmawa uno, chifukwa palibe yemwe amazifuna izo. Ndipo likanakhoza kukhala vuto la kuzikwirira izo. Koma inu mukumudziwa mmodzi aliyense wa iwo; Inu mukudziwa ubweya uliwonse umene uli mu thupi lawo. Inu mukudziwa tsitsi lirilonse limene liri pa mutu pawo.

¹²⁶ O Ambuye, yankhani pemphero. Muwalole iwo akhale otsimikiza, mmawa uno, kuti Inu ndinu Mulungu, ndipo Uwo ndi Mzimu Wanu. Mulole kupusa ndi chinyengo cha chipembedzo cha tsiku lamakono lino zichoke kwa iwo, zakuti, “O, ine ndine wa mpingo *wakuti wakuti*.” Mulungu, mulole izo zizimirire kuchoka ku malingaliro awo, pakali pano. Mu mphindi imodzi iyi, muwalole iwo agwire kuwonekera kwa Moyo Wamuyaya. Ndiyeno iwo afunafuna ndi kukhalira njala ya Iwo, kuti adziwe chimene Mulungu ali, ndipo iwo ali otsimikiza kuti Iye ali. Iye amasunga Mawu Ake.

¹²⁷ Kwa wochimwa, mulole iwo alape mwamsanga, akhale okonzekera ubatizo mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo inu munalonjeza kuti Inu mudzawapatsa iwo Mzimu Woyera. Inu munanena izo, Ambuye. Inu musunge lonjezo Lanu.

¹²⁸ Alipo wobwerera mmbuyo yemwe akutsimikiza kuti Inu ndinu Mulungu, ndipo iwo asochera kutali. Muwalole iwo abwere lero, chifukwa inu munati, “Ngakhale machimo anu akhale monga mlangali, iwo adzakhala oyera monga chisanu. Ofiira monga kapezi, iwo adzakhala oyera monga ubweya.”

¹²⁹ Ndipo ngati pali iwo amene ali odwala, muwalole iwo azindikire kuti Ndinu Mulungu. Inu mumasunga Mawu Anu. Inu muyenera kumasunga Mawu Anu. Pamene iwo akudzigoneka okha, ali ndi Mafuta, Mzimu umene uli mkati mwa iwo amene akuvomereza kuti iwo akukhulupirira. Ndiyeno, iwonso, ali ndi Mawu, Mkate wa Moyo umene wafalikira, Khristu; khazikitsani mwa iwo, mwa Chipangano Chakale; ndi mwa Chipangano Chatsopano, kuti musonyeze kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Muwalole iwo kuti asakanize Mawu amenewo ndi Mafuta, Mzimu, zimene iwo ali nazo, ndiye aime pa mapazi awo pa guwa, akuti, “Izi ndi zonse zimene ine ndiri nazo, Ambuye. Ine ndikuzibweretsa izo.”

O, momwe Inu muti muzichulukitsire! Momwe izo ziti ziyitanire Mulungu wambiriyakale powonekera! Momwe izo ziti zimupangitse Yehova kuwuka, ndi mtima wofufuma, kuti, “Ine ndiri naye mwana yemwe amandimvera Ine. Ine ndamuyika iye kupyola mmayesero, ndipo iye akutsimikizira kuti iye amandikonda Ine ndipo iye akundikhulupirira Ine. Iye akutsimikiza kuti Ine ndine.” Pakuti iwo anati, “Iye amene abwera kwa Mulungu ayenera kukhulupirira kuti Iye ali, ndi wopereka mphoto kwa iwo amene amufunafuna Iye

modzipereka.” Perekani izo, ora lino, pamene ife tikupereka izo kwa Inu.

¹³⁰ Ndipo, tsopano, pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa. Ndipo iwo amene ali nkusowa kwa chirichonse, kodi inu mungaima pa mapazi anu, amene mukufuna kuyika. . . Tsopano, ngati inu simuli kutsimikiza kuti Iye ndi Mulungu. . . Ngati inu mukutsimikiza kuti Iye ndi Mulungu, Iye asunga lonjezo Lake, chipulumutso, machiritso, chirichonse chimene chiri, ngati inu mukutsimikiza kuti Iye ndi Mulungu, imani pa mapazi anu. Ngati inu muli ndi winawake yemwe inu mukufuna kuti mumupempherere, imani pa mapazi anu. Ngati ndinu—ngati ndinu wotsimikiza kuti Iye ndi Mulungu, pangani chopempha chanu chidziwike mu kusunkhana kwa overa. Inu mukuchita izo pamene inu mukuyima. . . [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

“Ine ndikutsimikiza kuti Iye ndi Mulungu. Ine ndikukhulupirira kuti Iye amasunga Mawu Ake. Ndipo ine ndikutsimikiza kuti chopempha changa. . . Ine ndikuchiyika icho pansa pa Magazi, pakali pano.” Ngati inu muchita izo, ikani tchimo lililonse. Tchimo lililonse ndi kusakhulupirira. Inu mukhoza kukhala membala wa mpingo, koma ine ndikutanthauza *tchimo*, “kusakhulupirira” kwanu. Inu mukuliyika ilo pansa ngati nsembe. Inu mukuti mulipereke nsembe ilo. Inu mukubwera ku mtanda. Inu mukuti mupereke nsembe, tsopano, kusakhulupirira kwanu konse. Ndi kukupereka iko kwa Iye, ndi kudziwa kuti Iye ali, ndipo ndinu wotsimikiza kuti Iye ayankha. Ngati inu muli wa izo, kwezani mmwamba dzanja lanu. Khalanibe mwanjira imeneyo.

¹³¹ Ambuye, Inu ndinu Mulungu. Pano pali Mafuta awo ndi Chimanga chawo, zitasakanizidwa limodzi. Iwo akuzibweretsa Izo ku mtanda, kumene Moto wa Mulungu uti ugwere mu mitima yawo (ngati iwo akutanthauza kwenikweni izo) ndi kuidya nsembe imeneyo. Inu musunthira powonekera, kwezani madzi achikopa. Kubwera kuchokera Kumwamba, mu galeta wa Moto. Inu mugwedeze miyamba yonse ndi dziko lapansi, kuti muwapatse iwo mphoto.

¹³² Pamene iwo ayima ndi manja awo atakwezedwa mmalere, kusonyezera kuti iwo akukhulupirira, ndipo iwo adziyika okha, ndi chopempha chirichonse chimene iwo ali nacho, pa guwa Lanu pomwe. O Mulungu wa Kumwamba ndi dziko lapansi, Woweruza wa Miyamba ndi dziko lapansi, ndithudi Woweruza wa Kumwamba ndi dziko lapansi apereka chirungamo. Ndithudi Iye asunga Mawu Ake, Inu Amene mumadziwa mitima ya amuna, mitima ya akazi, mitima ya anthu awa.

¹³³ Ambuye Mulungu, ine ndikuyika manja anga omwe mmwamba, pakuti ine ndikudziwa kuti ine ndiri nako kusintha kwa utumiki tsopano. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti Inu muli. Ine ndakuwonani Inu mutaima kutali mu Lawi la

Moto. [M'bale Branham akugogoda pa guwa katatu—Mkonzi.] Ine ndakuwonani Inu mukufufuza zinsinsi za mitima ya anthu. Palibe nthawi imodzi imene Inu munalepherapo. Inu munalonjeza izo pamene Inu munapanga izo kutaliko, kuwoloka msewu kuno, pamene Inu munayamba poyamba kuchita kuti muzichita zinthu izi. Ndipo Inu mwanditeteza ine kuzungulira dziko, ndi kuzungulira ndi kuzungulira. Ine ndiri wotsimikiza kuti Ndinu Mulungu. Ine ndikutsimikiza za izo.

¹³⁴ Ine ndikudzipereka ndekha ndi anthu awa, ndi nsembe ya onse amene ine ndiri nawo, Ambuye, kwa Inu, kwa utumiki. Ine ndiri kuyamba kachiwiri, Ambuye, kuyenda kuzungulira dziko. Ndithandizeni ine, O Mulungu. Ngati ine sindinakuhulupirireni Inu pa nthawi iliyonse, mundikhululukire ine pa machimo anga. Mundikhululukire ine pa kusakhulupirira kwanga. Ine ndikudziwa kuti Inu muli, ndi wopereka mphotho kwa iwo amene akufunani Inu.

¹³⁵ Monga chomwecho, ine ndikuvomereza machimo a anthu anga, mmawa uno, kufooka kwawo ndi kukaikira kwawo, pamene iwo aima ndi mikono yawo mu mlengalenga. Ine ndikuvomereza machimo awo, Ambuye, ndi zooka zathu zonse. Tumizani Mzimu Woyera pa ife, ndi chisindikizo cha kuvomereza Kwanu, kuti Inu ndinu Mulungu. Ndipo Inu muli pano tsopano kuti mutilandire ife, ndi kuti mutitengere ife mu mikomo Mwanu, ndi kuti mutiwombole ife pa chirichonse chimene ife tachitaya. Ngati liri thanzi lathu, mulole ilo libwezeretsedwe kwa mazana. Ngati iyo ili solo yathu, mulole iyo ibwere kwa ife munga chinthu chowala, chonyezimira, yodzazidwa ndi Mzimu Woyera, kuti chiperekedwe pamaso pa Mulungu. Ngati iko kuli kusakhulupirira, mulole iko kubwere kwa ife kachiwiri, Ambuye, ndi chikhulupiriro choti nkusuntha mapiri. Perekani izo, Ambuye.

¹³⁶ Ife tikukhulupirira kuti Inu mukusuntha, Mzimu Woyera ukulowerera mnyumba monse muno, pa anthu awa, ndi mmitima mwawo, kuwasuntha iwo kuti alandire Mulungu wamoyo. Izi ife tikuchita mu Dzina la Yesu Khristu.

Chikhulupiriro changa ncha kwa Inu,
Mwanawankhosa wa Kalvare,
Mpulumutsi Waumulungu;
Ndimveni ndikupemphera,
Chotsani machimo anga,
Msandilore ndisochere
Kuchoka kwa Inu.

¹³⁷ Kodi inu mukutanthauza izo? Kodi inu mukuzilandira izo? Kwezani dzanja lanu, ndi kuti, “Ine tsopano ndikulandira izo. Ine ndikukhulupirira.”

Mnjira ya moyo nkayenda,
 Zokwiyitsa pondizinga,
 Khalani Namulondola wanga;
 Ingitsani mdima ukhale usana,
 Pukutani chisoni mantha achoke,
 Msandirole ndisochere
 Kuchoka kwa Inu.

Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu.

¹³⁸ Utatha Uthenga wolimba, wodula-molimba uwu; wamwano, ndipo utabweretsedwa mwa njira yankhaza, koma iwo ndi Choonadi. Ndipo ngati inu mutakhulupirira modzichepetsa zimene inu mwazipempha, kuti inu mulandira, inu musalole konse chirichonse chikukankheni inu kuchoka ku msewu wowongoka uwo. Imani pomwepo. Ziribe kanthu kuchuluka kwa momwe ndalalikira, chirichonse chimene ine ndingachite, kapena chirichonse chimene munthu aliyense angati achite, izo sizidzakhoza konse kukhala ndi mphamvu mpaka inu mutavomereza izo ngati chuma chanu chanu.

¹³⁹ Inu mukhulupirire izo ndi mtima wanu wonse, chirichonse chimene inu mwachikhumba. Ngati inu mwalapa machimo anu, Mulungu wakukhululukirani inu. Inu musati mukaikire konse izo kenanso. Ngati ndinu wobwerera mmbuyo, inu mwatengedwa kubwerera, mmawa uno. Ngati inu mukusowa Mzimu Woyera, ndiye mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha tchimo lanu. Ndiwo Mawu a Mulungu. Iye sangati awasinthe Iwo kwa mpingo uliwonse, palibe chipembedzo, kapena wina aliyense ayi. Izo ziyenera kukhala mwanjira imeneyo. Ife tiyenera kukomana ndi zofunikira zake, osati zofunikira za mpingo, zofunikira Zake. Ndicho chimene ife tiyenera kuchita.

¹⁴⁰ Iye anati, “Pemphero la chikhulupiriro lidzapulumutsa wodwala.” Ngati inu mukudwala, ine ndipemphera pemphero la chikhulupiriro kwa inu. Inu mupemphere ilo mu mtima mwanu momwe. Ndipo khulupirirani izo, vomerani izo, imani nji pa izo. Izo ziyenera kukhala mwanjira imeneyo. Palibe chimene chingatenge izo, ziribe kanthu momwe izo zikuwoneka zolunda.

¹⁴¹ Inu mukuti, “Chabwino, izo zikhoza kumawoneka ngati kuti ine ndikanali wodwala.” Izo ziribe... Ndi mapiko chabe a Angelo atasonkhana pamodzi. Ndizo zonse. Ndi Mulungu mu mawonekedwe a dalitso. Izo zikuwoneka zolunda kwa inu. Yandikirani pang’ono kwa izo ndipo yang’anani pa izo kachiwiri, muwone ngati izo si Mulungu ataima pamenepo, akusunga Mawu Ake.

¹⁴² Tsopano pamene ife tiri ndi mitu yathu itaweramitsidwa, ine ndifembenezira msonkhanowu kwa M’bale Neville, m’busa wathu.



KHALANI OTSIMIKIZA ZA MULUNGU CHA59-0125
(Be Certain Of God)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikidwa mu Chingelezi pa Lamlungu mmawa, pa Januwale 25, 1959, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 1999 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©1999 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org